# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## NTHAMBI YOONA ZA NYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO


### ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'DZINJA LA 2025 - 2026, M'BOMA LA MULANJE

## DZINJA LA 2025 – 2026 MWACHIDULE

Katenthedwe ka Nyanja ya mchere ya Pacific sikakhudza kwambiri nyengo ya dzinja ya 2025 – 2026.


Boma la Mulanje likuyembekezeka kulandira mvula ya mulingo wokhadzikika mu dzinja la 2025/2026.

## October 2025




Madera ena abomali akuyembekezeka kulandila mvula yosapyola mulingo wa 50mm. Komabe mvula ya chidzimalupsa ya mphepo ya nkuntho ndi mphezi yikuyambekezeka.

## November 2025





Mvula ya mulingo wokhazikika kapena kuchepera apo ikuyembekezeka m'bomali mu November.

Madera ochuluka m'bomali akuyembekezera kulandila mvula yapakati pa 50 mm ndi 150mm.

Mvula yokhazika m'bomali ikuyembekezeka kugwa kuyambira mu sabata la chitatu la November, 2025.

M'bomali liyembekezere mphepo ya nkuntho ndi mphenzi mweziwu.


## December 2025




Madera ambiri m'bomali ayembekezere kulandila mvula ya pakati pa 200 mm ndi 250 mm ndipo madera ena ochepa monga kuvuma kwa dera la T/A Mabuka komanso ku zambwe kwa dera la SC Laston Njema ayembekezere kulandila mvula ya mlingo wa 300 mm.

Ng'amba yosapzora masiku asanu ndi awiri ikuyembekezeka mu February, 2026.


## January 2026




M'mweziwu bomali likuyembekezera kulandila mvula yochuluka. Madera ena ayembekezere kulandira mvula ya pakati pa 350 mm ndi 400 mm a kwa T/A Mabuka, Mulanje boma, ndi Mulanje Mountain Reserve. Komabe, madera ena akuyembekezera kulandila mvula yapakati pa 250mm mpaka 300mm


Pali kuthekera kokhala ndi ng'amba yosapitirira sabata imodzi mu January.

## February 2026




Madera ambiri m'bomali ayembekezere kulandila mvula ya pakati pa 200 mm ndi 250 mm ndipo madera ena ochepa monga kumvuma kwa dera la TA Mabuka komanso ku zambwe kwa dera la SC Laston Njema akuyembekezere kulandila mvula yokwana 300mm. Chiopsezo cha ng'amba yosapyora masiku asanu ndi awiri ndi chachikulu mu February, 2026 m'bomali.

## March 2026





Mvula ya mlingo wokhazikika kapena kuposera apo ikuyembekezeka mu March, 2026.

Mvula ya mlingo wa pakati pa 250mm ndi 300mm, ikuyembekezeka kugwa m'madera a kwa SC Laston Njema ndi Mulanje Mountain Reserve.

Madera ena ambiri ayembekezere mvula ya mlingo wa pakati pa 200 mm ndi 250mm.

## April 2026





Mu April, madera ozungulira nkhalango ya phir la Mulanje , SC Laston Njema, TA Mabuka ndi Mulanje boma ayembekezere mvula ya mulingo wa pakati pa 100 mm ndi 150 mm pomwe madera ena onse a m'bomali ayembekezere kulandila mvula ya mulungo wa pakati pa 50 mm ndi 100 mm.

Nyengo ya dzinja m'bomali ikuyembekezeka kutha mu sabata ya chinayi ya mwezi wa April, 2026.

- Boma la Mulanje likuyembekezeka kulandira mvula ya mulingo wokhadzikika
- Mvula yokhazikika ikuyembekezeka kugwa kuyambira mu sabata lachitatu la mwezi wa November, 2025.
- Nyengo ya dzinga ikuyembekezeka kufika kumapeto sabata lachinayi la mwezi wa April, 2026.
- Nyengo ya dzinja m'bomali ikuyembekezeka kukhala yotalika masiku a pakati pa 150 ndi 160 .
- Ng'amba yokwana sabata imodzi mu January komanso February, 2026 ikuyembekezeka.

| MIMOSA | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 19.5 | 69.2 | 29.5 |
| NOV | 98.4 | 138.7 | 73.1 |
| DEC | 188.7 | 329.7 | 228.8 |
| JAN | 223.7 | 401.1 | 353.6 |
| FEB | 214.1 | 271.1 | 202.6 |
| MAR | 166.8 | 291.2 | 258.3 |
| APR | 65.0 | 160.8 | 106.5 |




**Ulosiwu udzaunikidwanso mu December 2025**

For further information contact: The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw

Zapangidwa ndi kutsindikizidwa ndi thandizo lochokera ku: